NYA_TTB_1066_SCRIPT

2 Petro : 2:5-9

Mutu : Chiphunzitso chonama chimadza ndi aphunzitsi onyenga.

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyamba ndi mau opezeka pa Yesaya 42:16, amene akuti, "Ndipo ndidzayendetsaakhungum'khwalala limene iwosalidziwa; m'njira zimene iwo sazidziwandidzawatsogolera; ndidzawalitsira mdima m'tsogolo mwawo ndi kulungamitsa malo okhota. Zinthu izi, Ine ndidzachita, ndipo sindidzawasiya."

Tsono mupologalamu yapita ija, tinali kusanthula 2 Petro 2:4-6, momwe timakambirana pamutu wakuti chiphunzitso chonama chimadza ndi aphunzitsi onyenga. Ndipo lero pa 2 Petro 2:5-9, tipitiliza kusanthula mutu womwewo wakuti chiphunzitso chonama chimadza ndi aphunzitsi onyenga.

5. Ndipo sanalekerera dziko lapansi lakale, koma anasunga Nowa Mlaliki wa chilungamo, ndi anzake asanu ndi awiri, pakulitengera dziko la osapembedza chigumula.

Pamene tidzalowa m'chapter 3, tidzapeza kuti Petro akukamba za maiko atatu, awa ndi; dziko lomwe linalipo kale, dziko lomwe lilipo pakali pano ndipo dziko lomwe lidzakhala m'tsogolomo.Ndiye pano Petro akukamba za dziko lomwe linalipo m'nthawi Nowa. Petro akunena kuti m'nthawi yake Mulungu adapulumutsa Nowa, munthu wachisanu ndi chitatu, amene analalikira chilungamo kwa nthawi yaitari, pamodzi ndi ena asanu ndi awiri. Awa, anali ana ake atatu a amuna, akazi awo ndi mkazi wake, anthu amene anapulumukakuchigumula cha mvula. Tsono nkhani ikuchoka pakuti anthu nthawi imeneyo anali achipembedzo ndithu, koma anasiya kupembedza Mulungu woona, nayamba kukhala m'moyo monga ngati kuti kulibe Mulungu.Kutanthauza kuti anthu awa, anali kukhala m'moyo wofuna kukwaniritsa zokhumba za thupi. Moyo uwu, ndiwo unautsa mkwiyo wa Mulungu ndipo ichi, ndichimene chinadzetsa mkwiyo wa Mulungu kuti aononge dziko la anthu wosalungama. Tere Paulo anafika potsimikizadi mtima, nanena pa Aroma 7:18, kuti, "Pakuti ndidziwa kuti m'kati mwanga, ndiko m'thupi langa, simukhala chinthu chabwino…"

Nowa anakhala m’nthawi yomwe anthu anaukira Mulungu, popeza munthu aliyense anali kuchita monga afuna.Kunena kuti nkhani yophana, siinali bvuto ndipo ichi, ndichimene chalowa m’dziko lathu lino. Ndiye pa Genesis 6:5, Mose akunena kuti, “Ndipo anaona Yehova kuti kuipa kwa anthu kunali kwakukuru pa dziko lapansi, ndiponso kuti ndingaliro zonse za maganizo a mitima yawo zinali zoipabezokhazokha.” Pachifukwa ichi, Mulungu anadza ndi chilango cha madzi a chigumula ndi kuononga dziko limenelo.Ili, ndidziko lomwe linali losayeruzika kupatula banja la munthu m’modzi.

Wokondedwa anzanga apaulendo ine, ndikuona kuti Mulungu anachita bwino kupereka chilango chimenechi, chifukwa anali kuona dziko la m’tsogolo. Ndiye tikunena kuti chilango chomwe anaperekacho, chikusonyezadi kuti Mulungu amasamalira moyo wa munthu umene adaulenga yekha. Ndikunena mau amenewa chifukwa chitatha chigumulachi, Mulungu pa Genesis 9:6, adaika lamulo lomwe likuti, “Amene akhetsa mwazi wa munthu, ndi munthunso mwazi wake udzakhetsedwa: chifukwa m’chifanizo cha Mulungu Iye anampanga munthu.” Ndiye ndi lamulo ili, kodi ife

tikuchita bwino kukangana naye Mulungu palamulo lomwe likuti, musaphe? Taonani wokondedwa kuti lamulo ili, likunena za munthu amene waika mkwiyo m'moyo wake, ndiye pofuna kukwaniritsa zofuna za thupi lake, amapha munthu wina. Tikunena kuti Mulungu anapereka mphamvu ku Boma, kuti liyenerakunyonga munthu amene akupha mnzake mwadala. Ndiye pano, tikunenetsa kuti pamene inu munyozera lamulo ili, ndiye kuti simukulabadira kufunika kwa moyo wa munthu, pamene inu mulemekeza munthu amene akulephera kuona kufunika kwa moyo wa mnzake, pakupha mnzake pofuna kukwaniritsa zofuna zake zoipa.

Tikunena kuti dziko lero likuona moyo wa munthu wakupha mnzake kuti ndiwo wofunika kwambiri kuposa munthu wophedwayo. Nkhani ikuti munthu wakupha mnzake ndiye akuchitiridwa chifundo popeza ndiye munthu, akusiyana ndi munthu wophedwamwadala uja. Ndikunena mau amenewa chifukwa munthu amene wapha munthu mnzake sasowa ma lawyer omuyimira mlandu wake komanso oweruzawo ndiwo amene amaonetsadi mtima wachifundopamunthuwopha mnzake. Tere,

pachifukwa chimenechi, lero kwathu kuno tikuona kuti anthu achifwamba ndiwo amene akuyendamomasukam'mizinda ndi m'midzi pamene anthu wokhulupirika akufera kundende.Komanso anthu amene sali omangidwaakufera m'ndende za nyumba zawo. Kutanthauza kuti munthu amene ali ndi nyumba yake ndiye kapolo popeza sangathe kuturuka ngakhale aone wakubaakutenga mbuzi yake. Ndiye inu mukaona chimenechi, bvuto lathu ndichiyani? Ine, ndikuona kuti atsogoleri athu, amene sadziwa kapena kulabadira Mulungu ndiwo amene sangabvomerezekunyongedwakwa anthu akuphaanzawo. Ndiye pachifukwa chosaopa Mulungu, munthu wina aliyense ali ndi ufulu wakuledzera, kuchita chigololo, kupha, kuba ngakhalenso kukwatirana amuna ndi akazi wokha-wokha, popeza palibe amene angawaphunzitse za kuipa kwa zimenezi. Ichi, ndichifukwa chake matenda a HIV/Aids sadzatha, m'dziko lathuli ngati Bomasilingayambe kulemekeza malamulo a Mulungu.

Nkhani ikuti, anthu wosapulumutsidwa, ayenera kulandira chilango kuchokera ku Boma, koma ngati sizingatero ndiye kuti dziko lathu likugwamosakaika konse.Mwachisoni kuti dziko

likuonongeka pamene Mulungu anaperekeratu lamulo lomwe likhozakutithandizakuturukam'bvuto limeneli.Kutsimikiza kuti moyo wosapembedza Mulungu woona, ndiwo umene umachotsa munthu pachitetezo cha Mulungu ndi kumuika poyera kuti aonongeke.

6. Ndipo pakuisandutsamakara midzi ya Sodomo ndi Gomora anaitsutsapoigwetsa, ataiika chitsanzo cha kwa iwo akukhala osapembedza.

Ndime ino, ikuonetsa chitsanzo cha momwe Mulungu anachitira ndi midzi ya Sodomo ndi Gomora, ngakhale midziyi inali m'dera lomwe nthaka yake inali yachonde.Tsono nkhani ikuti ngakhale malo akhale achonde, Mulungu akhoza kulisandutsa dera losabala ndipo dera la madzi ochuluka kukhala dera lapfumbi ndi phulusa.Kutsimikiza kuti palibe Boma lomwe lingateteze anthu ochimwa kuti asalandire chilango cha Mulungu. Pano tikuona chitsanzo cha Sodomo ndi midzi ina yozungulira kuti siinalandirechitetezo kuchokera ku maBoma awo, monga muja analandira chilango angelo amene anali ambiri komanso aulemu wawo.

Tere pano taona kuti Mulungu anagwiritsa ntchito madzi ndi moto kuononga dziko lakale ndi midzi ya Sodomo ndi Gomora.Kutanthauza kuti Iye amene asunga madzi ndi moto kuti ana ake asaonongeke, akhoza kugwiritsa ntchito zomwezi kuononga adani ake.Kutsimikiza mau a Yesaya 43:2, amene akuti, “Pamene udutsa pamadzi ndiri pamodzi ndi iwe; ndi poolokamitsinjesidzakukokolola; pakupyolapamotosudzapsya; ngakhale lawisilidzakutentha.” Ndiye tiyenera kuphunzira kuti anthu oipa ayenera kuyembekeza kulangika kwakukuru ndipo kuti chilango cha m’nthawi yakale chinaperekedwa kuti chikhale chitsanzo kwa iwo akubwera pambuyo pawo.

Nkhani yonseyi ikuchoka pankhani yomwe idalembedwa pa Genesis 19.Ndiye tikuona kuti Mulungu anagwetsa chilango pa Sodomo ndi Gomora chifukwa cha anthu anali kufuna kukwaniritsa zilakolakozathupi. Taonani tchimo lathupi lomwe linakula kwambiri ndi ukwati wa amuna ndi akazi okhaokha, komanso m’chitidwe wadama. Uwu, ndiwo m’chitidwe umene unabvomerezedwanso m’dziko lathu lino, kotero kuti anthu amenewa ali ndi ufulu kukhala ndi kuyenda paliponse m’dziko lino.

Koma tiyenera kudziwa kuti tchimo lathupindiloipa kwambiri. Inu ndi ine, tiri ndi umuthu wathu wakale ndipo ndiumunthu umenewu, umene umaonetsa kuipa kwenikweni kwa tchimolo. Ndikunena kuti ngakhale tchimo logonana amuna kapena akazi okhaokhalitamachitikapoonetsera, kodi likhoza kukhala lolemekezeka?

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna titsirize ndi mau akuti, pamene anthu adzitsitsa kapena kuti kudzinyoza motere, koposa garu, Mulungu akulonjeza kumtaya munthu wotereyu. Iyi, ndiyo nkhani yomwe Paulo akukamba pa Aroma 1:18-32. Tikunena kuti popeza dziko likusekerera pa tchimo ili, zapangitsa kuti m'chitidwewu, uchuluke m'dziko lathu lino. Tsono Uthenga ukuti, inu ndi ine, tiyenera kukhala maso pazitsanzo zonse momwe Mulungu akubwezera chilango kwa anthu onse amene anachoka pamaso pake nalowa muchonyasa chilichonse. Tere, tiyenera kudziwa kuti anthu onse amene akhala ndi kuyenda m'moyo wachisawawa, ayenera kudziwa chomwe adzakumana nacho posachedwapa, ngati apitilira kukhala m'moyo wotere.Ndiye zinthu

zonsezi zikuperekedwa kuti zikhale zitsanzo kuti zitithandize kupewa chilango chomwe chikudza mosakaika konse.

7. Ndipo anapulumutsa Loti wolungamayo, wolema mtima ndi mayendedwe onyasa a oipa aja
8. (pakutiwolungamayo, pokhala pakati pawo, ndi kuona ndi kumva zawo, anadzizunzira moyo wake wolungama tsiku ndi tsiku ndi ntchito zawo zosayeruzika).

Pano ndifuna kuyamba ndi mau akuti pamene Mulungu atumiza chionongeko pa anthu oipa, amalamula kuti olungama m'menemo aomboledwe.Ndikunena kuti ngati angatumize kapena kuthira moto kuti ukaonongemalowo, Iye (Mulungu), amaphimba mitu ya anthu wolungama kuti isaonongeke pamodzi ndi ya anthu oipa.Petro akupereka chitsanzo cha Loti kutianawerengedwa munthu wolungama pamaso pa Mulungu pakuona makhalidwe ake ndi zomwe zinali kutuluka pakamwa pake.Kutanthauza kuti Mulungu amamutenga munthu kukhala wolungama osati chifukwa cha ntchito imodzi yokha, koma chifukwa cha makhalidwe a moyo wake.Apa, tikuonakuti ngakhale Loti anakhala pakati pa anthu

osalungama, koma anayenda m'moyo woongoka.Koma uchimo wa anthu ena, unali ndi zotsatira pamoyo wa Loti.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti pamene munthu akhala pakati pa chibvundi, amakhudzidwa m'njira ziwiri; mwina amagwa muuchimo waanthuwo, kapena amamva chisoni chachikulu. Tikunena kuti uchimo wa anthu ena, uyenera kukhala chinthu chodzetsachisoni mwa anthu wokhulupirira ndipo ngati sitingamve chisoni, sitingathe kukhala wolungama. Tere, Loti ndiye chitsanzo amene anabvutika mumtima mwake kawirikawiri, pamene anali kuona zonyasa zikuchitika pakati pa anthu am'mudzi mwake. Kodi inu, mumamva bwanji pamene anthu a m'mudzi, m'dziko ngakhalenso mumpingo wanu akhala m'moyo wachitaiko?

Tsono ngakhale Loti anali kuona zonyasa zonsezi tsiku ndi tsiku, iye sanakopeke ndi kuyamba kuchita nawo zimenezi ayi.Kuchitira umboni mau amene a Paulo pa Afilipi 1:27, amene akuti, "Chokhachi, mayendedwe anu ayenere Uthenga Wabwino wa Kristu: kuti, Ndingakhale nditi ndirinkudza ndi kuona inu, ndingakhale nditi ndiri kwina, ndikamva za kwa inu, kuti

muchirimika mu Mzimu umodzi ndi kugwirira pamodzi ndi moyo umodzi chikhulupiriro cha Uthenga Wabwino.”

Loti, ndiye munthu amene Mulungu adamupulumutsakuchilango chomwe chinagwera anthu onsea m’mudzi wake.Ndiye pachifukwa chimenechi, tikunenetsa kuti Mulungu amadziwa momwe angapulumutsire ana ake ndi kulanga adani ake nthawi yomweyo.

Tsono ndifuna muone kuti Loti anali kumva zinthu zonyasa kawirikawiri ndipo Mulungu sanalolekuti mwana wake apitilize kumva zonyasazoterekwanthawiyaitali, popeza zikhoza kumgwetsamumchitidwe woipa. Apa, ndipo pamene Mulungu adalamula Loti kuti atulukem’mudzimo kuti angaonongekerekumodzi ndi anthu woipawo. Kutanthauza kuti Mulungu amasiyanitsa pakati pa anthu woipa ndi anthu ake.Kunena kuti woipa amaonongeka ndipo amasunga anthu ake.Ichi, ndichimene 2 Petro 2:9, akunena kuti, “Ambuye adziwa kupulumutsa opembedzapoyesedwa iwo, ndi kusungaosalungama kufikira tsiku loweruzaakalangidwe.”Apa, ndipo pamene Loti anawerengedwa wolungama chifukwa anadzisunga iye mwini

posalowa pakati pa oipawo. Kutsindika kunena kuti nthawi yonse anakhala m'Sodomo, Loti anakhalabe wolungama.

Ndiye pali chinthu china chochititsa chidwiichi, ndichakuti pamene Mulungu anali kuturutsa Loti m'Sodomo, Abraham amene anapatukana naye Loti, sanali kumunyodola chifukwa chakuchocha pambuyo pake ayi. M'malo mwake, iye anali kupempherera Mzinda wa Sodomo popeza amafuna kuti Loti apulumutsidwekuzonyasazo. Taonani Abraham anali kupempha Mulungu kuti asaononge Sodomo ngati mungapezeke anthu makumi asanu wolungama.Ndiye Abraham anasiyakupembedzeraatafika pa anthu khumi, koma Mulungu anampulumutsa Loti popeza adamuona kuti anali wolungama.

Ndiye tikuonanso kuti mkazi wa Loti anaturuka nawo ndithu kuchoka m'Sodomo, koma anasanduka chulu cha mchere popeza anayang'ana m'mbuyo. Apa, ndikuganiza kuti inu mwafunsa kale kuti, kodi panali chifukwa chanji kuti mkazi wa Loti asanduke chulu cha m'chere? Yankho likuti iye anacheuka, kuyang'ana m'mbuyo.Koma chifukwa chiyani anacheuka? Yankho likuti ngakhale iye anaturuka mu Sodomo, koma mtima wake unali

muzinthu zomwe zinali kuchitika m'menemo. Komanso ine, ndikuona kuti mkazi wa Loti anayang'ana m'mbuyo chifukwa sanakhulupirira Mulungu kuti akhoza kuononga Sodomo. Taonani, Mulungu adaonongadimudziwo ndipo iye anasanduka chulu cha mchere.Phunziro lalikulu lomwe tingatolemo ndi lakuti, pamene Mulungu analanditsa Loti mu Sodomo, zikuimira mkwatulowa mpingo wa Kristu. Kutsimikiza mau akuti mkwatuloudzachitika chisanadze chisautso chachikulu, chilango chisanadze popeza Mulungu sadzalora kuti ana ake akalandire chilango. Ichi, ndicho chitsanzo chachikulu momwe tikuona mpingo kapena wokhulupirira akukwatulidwa kuti asaone chibvundi popeza iwo anakhala wolungama chifukwa cha chikhulupiriro chawo mwa Kristu.

9. Ambuye adziwa kupulumutsa opembedzapoyesedwaiwo, ndi kusungaosalungama kufikira tsiku loweruzaakalangidwe.

Mtumwi Petro mundime ino, akupereka chithunzi chakuti Mulungu akhoza kupulumutsa anthu ake, m'mayesero ngakhale m'masautso.Iye, alindinjira zabwino zomwe angalanditsire ana ake. Tikunena kuti Iye amapeza njira zolanditsira ana ake pamene

ifesitingaonepo njira. Kawirikawiri iyi, imakhala njira yomwe ifesitingayembekezerekupulumutsira munthu. Tikunena kuti nthawi zina akhoza kutumiza mngelo ndi kugwira dzanja la mwana wake monga anachita ndi Loti pomuturutsam'Sodomo. Nthawi zina Mulungu amangophwanya mphamvu za m'dierekezi kapena kutumiza anthu ena kulanditsa mwana wake, kapenansokumchotsa mwana wake m'dziko lonyasa kwambiri ndi kumtenga kupita naye Kumwamba.Mwanjira yomweyo Mulungu akhoza kusunga woipa kufikira tsiku la chionongeko. Iyi, ndiyo nkhani ija tidaona mu 2 Petro 2:4, pamene Petro adanena kuti, "Pakuti ngati Mulungu sanalekerera angelo adachimwawo, koma anawaponya kundende nawaika ku mayenje a mdima, asungike akaweruzidwe." Ndiye mwa chitsanzo cha angelochi, tikuphunzira kuti Mulungu akhoza kusunga anthu woipa, monga ngati kuwamanga ndi kuwaika m'ndende, pamene akusungidwira chilango chotsiriza. Tikunena kuti ngakhale anthu awa, ayenda motasabwanji, koma ali pansi paulamuliro wa Mulungu ndipo akuwasunga ndi cholinga chakuti akakumane ndi chilango chothera. Mwanjira ina tikunena kuti anthu wochimwa onse, ngati sangatembenuke mtima lero, ndiye kuti aweruzidwa kale kotero

kuti akudikira tsiku ilo, kuti akalandire chilango chawo. Kutanthauza kuti tchimo ndi chilango pa icho chokha; ndipo Gahena ndiwo malo komwe kukathera zonse.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna titsirize ndi kunena kuti Mulungu akusunga anthu ake ndi woipa womwe monga mwanjira zake zomwe ifesitingazidziwe komanso sitingazimvetse. Mulungu akudziwa kusiyana pakati pa woipa ndi wolungama, inu ndi ine, sitingathe kusiyanitsa.Tere, ndichifukwa chake adanena kuti zilekenizikulire pamodzi zidzaonekapokolola.Ndiye chomvetsa chisoni ndichakuti tirigu ndi namsongole zonse zikukulira pamodzi ndipo mau a Mulungu akufalitsidwa m'nthawi yomwe ino.Koma patsiku lina, Mulungu adzazipatula zimenezi, pamene adzabwera kudzatenga ake kuchoka m'dziko lino pamene woipa adzatengedwa ku chionongeko chamuyaya.Kodi inu ndinu yani; namsongole kapena tirigu?

Kwalerotilekeza pano. Ndipo tinali kusanthula 2 Petro 2:5-9, momwe timapitiliza kukambirana pamutu wakuti chiphunzitso chonama chimadza ndi aphunzitsi onyenga.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!